Baibulo ya ana
Ikupasilani

Samuele, Mnyamata-Mtumiki wa Mulungu

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Janie Forest
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: Lyne Doerksen

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Hana anali mkazi wabwino, wokwatiwa ndi Elikana, mwamuna wabwino. Onse ankalambira Mulungu komanso ankakomera mtima anthu ena. Koma panali chinachake chimene chinkasoweka pa moyo wa Hana. Iye ankafuna kukhala ndi mwana. O, momwe ankafunira mwana! Anadikirira ndikupemphera ndikuyembekeza ndikudikiriranso. Palibe mwana anabwera!



Chaka chilichonse, Hana ankapita kukalambira kuchihema cha Mulungu. Chaka china analonjeza Mulungu kuti ngati angamulole kukhala ndi mwana wamwamuna, adzam'patsa mnyamatayo kukhala mtumiki wa Mulungu mpaka kalekale.

Wansembe wokalamba Eli anaona Hana akupemphera. Anaganiza kuti Hana waledzera ndi vinyo chifukwa milomo yake inali kugwedezeka koma palibe mawu. Eli anadzudzula Hana!

Koma Hana anauza Eli za pemphero lake lopempha mwana komanso lonjezo lake kwa Mulungu. Eli anayankha kuti: "Pita mumtendere. Ndipo Mulungu wa Israyeli akupatse chopempha chako chimene wapempha kwa Iye." Mawu a Eli anapatsa Hana chiyembekezo.

Posakhalitsa Hana anasangalala kwambiri. "Yehova anamukumbukira" ndipo anayankha pemphero Lake. Iye ndi Elikana anali ndi mwana wamng'ono dzina lake Samuele (limene limatanthauza "Wakumva ndi Mulungu"). Koma kodi Hana anakumbukira Yehova ndi lonjezo lake kwa Iye?





Chaka chilichonse Hana anasiya kupita kuchihema. Oo Pepa! Kodi anali ataphwanya lonjezo lake kwa Mulungu? Ayi, Hana anali kuyembekezera mpaka Samuele atakula kuti azitha kukhala kuchihema n'kuthandiza Eli potumikira Mulungu. Kenako anapita naye kuchihema.

Mulungu analemekeza kukhulupirika kwakukulu kwa Hana. Pambuyo pa Samuele, Mulungu anam'patsanso ana ena aamuna atatu ndi ana aakazi aŵili. Chaka chilichonse, Hana ankapita kuchihema kuti akalambire Mulungu komanso kuti abweretse Malaya atsopano a Samuele.

Samuele sanali mthandizi yekha wa Eli. Ana a Eli, Hofeni ndi Pinehasi, nawonso ankagwira ntchito kumeneko. Koma iwo sanalemekeze Mulungu mwa kuchita zoipa, ndipo sanasinthe ngakhale pamene bamboo awo Eli anawachonderera. Eli anayenera kuwachotsa ntchito pachihema. Koma sanatero.

Tsiku lina usiku, Samuele anamva mawu akumuitana. Mnyamatayo anaganiza kuti ndi Eli akuitana. Iye anati: “Ndine pano.” Eli anayankha kuti: “Sindinaitane.” Izi zidachitika katatu. Kenako Eli anadziwa kuti Mulungu akufuna kulankhula ndi Samuele.

Eli anauza Samuele kuti: "Akakuitana, unene kuti, 'Lankhulani Yehova, pakuti mtumiki wanu akumva.'" Mulungu anamuitananso ndipo anapatsa Samuele uthenga wofunika kwambiri.

M'mawa mwake Eli anaitana Samuele. "N'ciani cimene Yehova wanena kwa inu?" anafunsa. Samuele wachichepere anamuuza zonse. Unali uthenga woopsa kwambiri—Mulungu anali kudzawononga banja lonse la Eli chifukwa Hofeni ndi Pinihasi anali oipa kwambiri.

Chenjezo la Mulungu linakwaniritsidwa. Pa nthawi imene ankamenyana ndi Afilisiti, ana awiri oipa a Eli anatsogolera Likasa la Mulungu pamaso pa asilikali a Isiraeli. Adaniwo analanda Likasa ndi kupha Hofeni ndi Pinihasi pamodzi ndi Aisiraeli ambiri. Eli atamva zimenezi anagwa pampando wake n'kuthyoka khosi lake n'kufa tsiku lomwelo.

Likasa la Mulungu linabweretsa mavuto kwa Afilisiti. Analiika m'kachisi wa Dagoni, mulungu wawo wonyenga. M'maŵa mwake, fano la Dagoni linali litagwa nkhope yake pansi. Afilisti ananyamula Dagoni m'mwamba – koma m'maŵa mwake iye analinso pansi. Pa nthawiyi Dagoni anathyoledwa.





Matenda ndi imfa zinafalikira pakati pa Afilisti. Kuti aone ngati Mulungu anali kuwalanga, Afilistiwo anatumiza ng'ombe ziwiri zokoka ngolo yokhala ndi Likasa. Koma anasunga ana a ng'ombe. Iwo anati: "Ngati ng'ombezo zikapita ku Isiraeli n'kusiya ana awo, tidzadziwa kuti Mulungu wachita zimenezi." Ndipo ng'ombe zinakwera!

Kenako Samuele, amene tsopano anali wachikulire, analankhula ndi Aisiraeli onse. "Mukabwerera kwa Yehova ndi mtima wanu wonse ... Anthuwo anamvera mneneri wokhulupirika wa Mulungu." Ndipo dzanja la Yehova linalimbana ndi Afilisti masiku onse a Samuele.

Samuele, Mnyamata-Mtumiki wa Mulungu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

1 Samuele 1-7

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16